

File 1985



AKRISTU ATHANDIZA AKRISTU ENA KUTI AKULE MWA KRISTU
Olemba Ndi: Gena Hampton
Baptist Publishing House, Lusaka, Zambia

COC
NYA

Momwe mungakonzere mndandanda wa zinthu zofunika kuti inu mupempherere.

TSIKU PEMPHERO LANGA YANKHO LA MULUNGU

AKRISTU ATHANDIZA AKRISTU ENA KUTI

AKULE MWA KRISTU

***BAPTIST PUBLISHING HOUSE
P. O. Box 31995
Lusaka, Zambia***

OLEMBA NDI: GENA HAMPTON

Zithunzi-thunzi zimene ziri mkatimu, zinalengedwa kucoka m' buku lolembedwa ndi Bambo W.B. MOORE mu buku lao loledwa:-

***KUPANGA ANTHU KUKHALA OPHUNZIRA A YESU
KRISTU***

MAU OYAMBA

1. Colinga ca bukuli ndi cakuti inu muphunzire kukhala monga KRISTU YESU mu moyo wanu. Mudzaphunzira-nso momwe inu mungathandizire anthu ena ndikuwatso-golera kuti akhale Akristu, ndikuwathandiza momwe iwo angakulire mu moyo wa Cikristu.
2. Gulu lanu likhale ndi anthu osapitilira pa awiri. Anthuwa akhale anthu omwe adzakomana pamodzi ndi kuphunzira za Buku Lopatulika pamodzi ndikugawirana za momwe Mulungu ali kuwacitira mu moyo wao sabata liri lonse.
3. Sabata liri lonse mudzakhala muli kusunga mau a m'Buku Lopatulika pamtima, kuphunzira Buku Lopatulika, KUPEMPHERA pamodzi ndikuphunzira momwe tingacitire UMBONI za uthenga wabwino kwa anthu ena. Mu-yenera kupanga LONJEZO LANU KWA MULUNGU.

NJIRA YA MAPHUNZIRO

1. Sabata liri lonse mudzasungira pamtima ma vesi awiri a m'Buku Lopatulika. Ma vesi amenewa mudzawalemba pa pepala lanu la maphunziro.
2. Mtsogoleri adzatsogolera pa nthawi ya mapemphero ndipo adzaona kuti inu munasunga ma vesi omwe munaphunzira sabata liri lonse ndipo ayenera kutsimikiza.
3. Muyenera kubwereza mau omwe munasungira pa mtima tsiku ndi tsiku kwa miyezi iwiri.

KUSANTHULA BUKU LOPATULIKA

1. Sabata liri lonse mtsogoleri wanu adzatsogolera maphunziro ozama a m'Buku Lopatulika. Mau ali pepala lanu la maphunziro.
2. Phunzirani lemba limodzi tsiku ndi tsiku ku nyumba kwanu. Lembani mayankho amafunso pa pepala lanu la maphunziro.
3. Muyeneranso kuyamba kuwerenga uthenga wabwino wa Yohane pa nthawi yanu ya cete tsiku ndi tsiku.

10. Pomwe ndiitana Yesu mu moyo wanga, ndili ndi moyo wosatha. Ndizindikira ici cifukwa ca: 1 Yohane 5:11-12 ikuti; "Ndipo uwu ndi umboni wakuti Mulungu anatipatsa ife moyo wosatha, ndipo moyo umene uli mwa Mwana wace. Iye wakukhala ndi Mwana ali nao MOYO; wosakhala ndi Mwana wa Mulungu alibe moyo. Tsono lembani 1 Yohane 5:11-12 munsu mwa mtanda.

Aefeso 2:8-9 “PAKUTI MULI OPULUMUTSIDWA NDI CISOMO CAKUCITA MWA CIKHULUPILIRO, NDIPO ICI COSACOKERA KWA INU, CIRI MPHATSO YA MULUNGU, COSACOKERA KUNCHITO, KUTI ASADZITAMANDIRE MUNTHU ALIYENSE.

6. Mulungu ali ndi lonjezo kwa munthu aliyense wokonzekera kumumvera ndi kumukhulupilira. Yohane 5:25.

Yohane 5:24 akuti, “INDETU, INDETU, NDINENA KWA INU, KUTI IYE WAKUMVA MAU ANGA, NDI KUKHULUPILIRA IYE AMENE ANANDITUMA INE, ALI NAO MOYO WOSATHA, NDIPO SALOWA M’KUPERUZA, KOMA WACOKERA KU IMFA, NALOWA MMOYO WOSATHA.

Lembani Yohane 5:24 monga mwacitsanzo cimene ciri pacithunzico.

7. Komatu kuti munthu alandire lonjezo la Mulungu ayenera kufuna kupulumutsidwa ndipo afunika kutsegula citseko ca mtima wace.

CIBVUMBULUTSO 3:20 ikuti, “TAONA, NDAIMA PAKHOMO NDI GOGODA, WINA AKAMVA MAU ANGA NAKATSEGULA PAKHOMO, NDIDZALOWA KWA IYE, NDIPO NDIDZADYA NAYE, NDI IYE NDI INE.”

Tsopano lembani mau awa Cibvumbulutso 3:20 ndikulemba mnzere monga kwalembedwa pacitsanzo cathu. Ndipo lembani mau awa MOYO WOSATHA.

8. MAFUNSO OFUNIKA KUFUNSA:
1. Kodi munatsegula citseko ca mtima wanu kuti Yesu alowemo?
 2. Kodi pali cifukwa cina comwe simungamulandire lero lino?
9. PEMPHERO LAKULANDIRA YESU KRISTU. “Ambuye wanga Yesu ndapota nanu bwerani mu m’mtima mwanga ndipo mukhale Mpulumutsi ndi Ambuye wanga conde mundikhululukire macimo anga onse ndi kundipatsa ine mphatso ya moyo wosatha.

MAPEMPHERO

1. Mtsogoleri wanu adzatsogolera pa nthawi ya mapemphero sabata liri lonse pomwe mwa sonkhana.
2. Muyenera kupeza nthawi yakuti mupemphere inu nokha tsiku ndi tsiku.
3. Kuseri kwa pepala lanu la maphunziro mudzapeza malo omwe mungalembe mosala mndandanda wa zomwe mufuna kupempherera pa nthawi ya MAPEMPHERO. Mtsogoleri adzakusonyezani momwe mungacitire.

KUCITIRA UMBONI

1. Ma vesi omwe musunga pa mtima sianu nokha, muyenera kuuza anthu ena.
2. Mtsogoleri adzalongosola momwe mungacezere anthu ena ndikuwacitira UMBONI.
3. Mudzaphunzira momwe mungajambulire ULALO WOLOZA KU MOYO WOSATHA DZANJA NDI MTANDA WA MOYO.

KUCITIRA UMBONI

1. Ici cithandiza kuti tidziwane wina ndi mnzace ndipo ndikofunika kuti aliyense apeleke mwacidule umboni wace.
 - a) Mufotokoze za munthu amene akuthandizani koposa mu moyo wanu Wacikristu.
 - b) Kodi munthuyo anakuthandizani motani?

PAMAPETO

1. Nchito yanu yoyamba ndikusunga malemba pamtima ndi kucita phunziro lanu loyamba.
2. Kambilanani za malo ndi nthawi yokumaniranapo.
3. Tsirizani ndi pemphero.

LONJEZO LANGA KWA MULUNGU

1. Ndidzapezeka ku misonkhano yonse ya gulu ili. Ngati sindidzatha kutero, ndidzaonana ndi mtsogoleri ndi kunkonza nthawi ndi malo oti tingakomane ndi iye mkati mwa sabata lomwelo.
2. Ndidzapeza nthawi ndi tsiku ya kuphunzira Buku Lopatulika, kupemphera ndi kusungira mau apamtima.
3. Ndine wokonzeka kuphunzitsa anzanga zomwe ndidzaphunzira.

TSIKU..... KUSAINA KWANGA.....
(Dzina lanu)

PHUNZIRO 1

MAU APAMTIMA: Aroma 3:23, Aroma 6:23

MAU A MULUNGU A PHUNZIRO LALERO: Mutu wa phunziro

Yohane 5:24 Iye wakumva mau anga, ndikukhulupilira anandituma Ine, ali

Yohane 10:27-28 Ndani angalande (kukwatula) nkhosazace kucoka ku dzanja lace?.....

Aroma 8:16 Mzimu yekha acita umboni pamodzi ndi mzimu wathu kuti tiri.....

Aroma 8:35-38 Adzatisyanitsa ndani ndi cikondi ca Kristu?.....

PEMPHERO: Kambilanani za mndandanda wa zofunikira ku pempherera. Pempherani pamodzi.

KUCITIRA UMBONI: Mtsogoleri aphunzitse kwa theka limodzi nkhani ya ulalo woloza ku moyo wosatha.

Aroma 3:23 ikuti, “PAKUTI ONSE ANACIMWA, NAPEREWERA PA ULEMERERO WA MULUNGU.”

2. Dipo la cimo limeneli ndi IMFA.

Aroma 6:23 ikuti, “PAKUTI MPHOTO YACE YA UCIMO NDI IMFA, KOMA MPHATSO YA ULELE YA MULUNGU NDIYO MOYO WOSATHA MWA KRISTU YESU AMBUYE WATHU” “Lembani Aroma 6:23 muni mwa citsanzo pa mwambapo.

3. Sitifuna KUFA ndi kuweruzidwa koma . . .

Ahebri 9:27 “NDIPO POPEZA KWA IKIKATU KWA ANTHU KUFA KAMODZI NDIPO ATAFI CIWERIRO.”

Lembani mau awa Ahebri 9:27. Langani mnzere monga mwa citsanzo ndikulemba mau awa: IMFA YAMUYAYA.


4. Yankho lilipo. Yesu Kristu amene adzatifera pa mtanda cifukwa ca macimo athu ndiyo njira yonkayo ya kwa Mulungu.

Aroma 5:8 “KOMI MULUNGU ATSIMIKIZA KWA IFE CIKONDI CACE CA MWINI YEKHA MMENEMO, KUTI POKHALA IFE CIKHALIRE OCIMWA, KRISTU ADATIFERA IFE.”

KRISTU ndi njira yokhayo imene munthu angafikire kwa Mulungu kudutsa dzenje lomwe liri pakati pa munthu ndi Mulungu. Kristu ndi njira ya mtanda. Anamanga ulalo pakati pa munthu ndi Mulungu. Lembani Aroma 5:8 monga pa mwambapo. Langani MTANDA kulumikidza munthu ndi MULUNGU monga mwa citsanzo ndikulembamo mau akuti KRISTU mkati mwa MTANDA modutsa.

5. Cipulumutso ndi mphatso ya ulere ya MULUNGU.

ULALO WOLOZA KUMOYO WOSATHA



1 YOHANE 5:11 12

1. Buku Lopatilka litiphunzitsa kuti MULUNGU akonda anthu onse ndipo afuna anthuwo amudziwe IYE.

Langani MUNTHU ndi MULUNGU ndi dzenje pakati pao lowalekanitsa wina ndi mnzace. Lembani liu komwe kuli munthu ndi liu komwe kuli MULUNGU. Ndipo lembani cimo litilekanitsa ndi Mulungu Aroma 3:23. Koma munthu analekanitsidwa ndi Mulungu cifukwa cakuti ana-cimwa.

PHUNZIRO 2

MAU APAMTIMA: Ahebri 5:8

Nenani mau apamtima munaphunzira sabata latha.

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: NTHAWI YA CETE

Masalmo 5:3 Ndi nthawi yanji pomwe anapemphera?.....

Marko 1:35 Ndi liti ndipo ndi malo otani Kristu anapemphera?

Luka 10:39 Ndi ciyani Maliya anasankha kucita?.....

Luka 11:9-10 Yesu Kristu akuuzani kucita ciani?

PEMPHERO: Lembani maina a abwenzi ndi anansi anu omwe ali otayika (sali a Kristu). Pempheperi pamodzi.

KUCITIRA UMBONI: Mtsogoleri aphunzitse theka lotsala za nkhani ya ULALO WOLOZA KU MOYO WOSATHA.

PHUNZIRO 3

MAU APAMTIMA: Aefeso 2:8-9; Yohane 5:24
Nenani mau apamtima a phunziro 1 ndi 2.

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: PEMPHERO

Ahebri 13:15 Tiyenera kupereka ciani kwa Mulungu?

1 Yohane 1:9 Tilandira bwanji cikhulukiro ca macimo anthu?.....

Aefeso 5:20 Ndi pa zinthu zotani tingayamikire Mulungu?

PHUNZIRO 4

MAU APAMTIMA: Cibvumbulutso 3:20; 1 Yohane 5:11-12

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: UMBUYE WA KRISTU

Afilipi 2:9-11 Ndi malilime onse abvomera kuti Yesu Kristu ndi.

Luka 9:23 Yesu anati tinyamule.....tsiku ndi tsiku ndi.....Iye.

Luka 6:46-47 Otsatira a Yesu ayenera kumvera mau ace ndi
.....

PEMPHERO: Pemphereranani mugulu lanu wina ndi mnzace.

KUCITIRA UMBONI: Phunzitsani nkhanu ya ULALO WO-
LOZA KUMOYO WOSATHA kapena kwa
ophunzira anzanu. Musanakumane sabata
lamawa phunzitsani nkhanu ya ULALO WO-
LOZA KUMOYO WOSATHA ku munthu ali-
yense. Mtsogoleri wanu akonze zakukacezera
anthu kawiri kawiri.

PHUNZIRO 5

MAU APAMTIMA: Bwerezani ma vesi onse a nkhanu ya za
ULALO WOLOZA KUMOYO WOSATHA.

**MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: LIU (LIU LA
MULUNGU) Mau**

Aroma 10:17 Cikhulupiliro cidza

Cibvumbulutso 1:3 Wodala iye amene

Cacitatu: Ndi KUSONKHANA ndi okhulupilira anzathu.
(Lembani mau awa: KUSONKHANA kudzanja la manja ndi
Yohane 13:35.)

Yohane 13:35 ikuti, "MWA ICI ADZADZINDIKIRA ONSE
KUTI MULI AKUPHUNZIRA ANGA, NGATI MULI NACO
CIKONDANO WINA NDI MNZACE."

Malo oyenera kwa ife kuti tikule mu Cikristu ndi mnyumba
ya MULUNGU mpingo ndipo tingathe kukumana ndi anza-
thu okhulupilira mwa Kristu.

Cacina: Mkristu ayenera KUCITIRA UMBONI ku dziko
lapansi. (Lembani KUCITIRA UMBONI kudzanja la manze-
re munga mwacitsanzo ndikulemba Yohane 15:8. Yohane
15:8 ikuti; MWA ICI ALEMEKEZEDWA ATATE WANGA,
KUTI MUBALE CIPATSO CAMBIRI: NDIPO MUDZA-
KHALA AKUPHUNZIRA ANGA.

4. Pomwe moyo wanu wayamba kupatsa zipatso mukhoza
kuyandikira ku anthu ena.

1. Kukhala mu MAU AMULUNGU zotsatira zace ndi ku-
phunzitsa (Lembani mau KUPHUNZITSA pansu pa mau a
MULUNGU.)

2. KUPEMPHERA NDI CIKHULUPILIRO cotsatira cace
ndi KUPEMBEDZA. (Lembani mau KUPEMBEDZA pa-
mwamba pa mutu mwa citsanzo.)

3. Kusonkhana ndi okhulupilira anzathu cotsatira cace ndi
KUTHANDIZA mu mpingo ndi kukula mwa Kristu (Le-
mbani mau KUTHANDIZA kudzanja la manja munga
mwa citsanzo.)

4. Kucitira umboni kudziko la pansu cotsatira cace ndi kula-
likira Uthenga Wabwino. Lembani mau KULALIKIRA
UTHENGA WABWINO pafupi ndi dzanja lamanzere
munga mwa citsanzo.

1. Wophunzira ndi munthu amene atenga KRISTU monga Mbuye wa moyo wace.

Luka 14:27 ikuti, 'NDIPO AMENE ALIYENSE SASE-NZA MTANDA WACE MWINI YEKHA SAKHOZA KUKHALA WOPHUNZIRA WANGA.

(Lembani mau; MTANDA WAMOYO pamwamba pa pepala lanu, mumsi mwa mauwo. lembani Luka 14:27.

2. Moyo wa Cikristu utanthauza KRISTU kukhala mwa inu. Agalatiya 2:19-20 akuti; "PAKUTI INE MWALAMULO NDAFA KU LAMULO, KUTI NDIKHALE NDI MOYO WOSATINSO INE AI, KOMA KRISTU ALI NDI MOYO MWA INE: KOMA MOYO WOMWE NDILI NAO TSOPANO MTUPI NDIRI NAO MCIKHULUPILIRO CA MWANA WA MULUNGU, AMENE ANANDIKONDA NADZIPEREKA YEKHA CIFUKWA CA INE."

Lengani cithunzi coyelekezera munthu. Lengani manja monga citsanzo ndipo mkati mwace lembani mtima ndikulembamo mau awa KRISTU, NDI AGALATIYA 2:19-20 monga mwa citsanzo.

3. Pali zinthu zina zomwe mkristu ayenera kucita kaya kutsata ngati afuna kutenga mtanda wace ndikufuna kutumikira anthu ena.

Coyamba: NDIKUKHALA MU MAU A MULUNGU. Lengani Buku monga mwaona pa citsanzo ndipo munthu wanuyo aimilire pomwepo ndipo lembani mau awa; Yohane 8:31. CIFUKWA CACE YESU ANANENA KWA AYUDA AJA ADAKHULUPILIRA IYE, NGATI MUKHALA INU M'MAU ANGA, MULI AKUPHUNZIRA ANGA NDITHU.

Caciwiri: KUPEMPERA MCIKHULUPILIRO (Lembani mau a PEMPHERO mkati mwa mutu ndi Yohane 15:7. "NGATI MUKHALA MWA INE, NDI MAU ANGA AKHALA MWA INU, PEMPHANI CIMENE CIRI CONSE MUCIFUNA NDIPO CIDZACITIKA KWA INU."

Masalmo 119:11 Ndi nawabisa mau anu

Masalmo 119:97 Ha! Ndikondadi canu.

Macitidwe 17:11 Tsiku ndi tsiku ndiyenera ku malemba.

Yakobo 1:22 Ndidzaika Liu Lace

Mukatsiriza kuwerenga uthenga wabwino wa Yohane mu nthawi yanu ya cete, yambani kuwerenga buku lina m'Buku Lopatulika. Mwachitsanzo; Marko.

PEMPHERO: Sankhani mnzanu wakuti muzipemphera naye sabata liri lonse.

KUCITIRA UMBONI: Gwiritsirani dzanja kusonyeza momwe tingakhali mu mau a Mulungu. Phunzitsani nkhanu ya ULALO WOLOZA KU-MOYO WOSATHA ku anthu awiri sabata lino. Pemphani thandizo kwa mtsogoleri wanu ngati nkofunika kutero.

PHUNZIRO 6

MAU APAMTIMA: Aroma 10:17; Masalmo 119:97

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: MPINGO NDI INU

Akolose 1:18 Ndipo iye Yesu Kristu ndiye mutu wathupi

Macitidwe 2:41-42 Ndi zotani zomwe a mu mpingo anacita?

Akolose 1:28-29 Mpingo uyenera kulalikira ku anthu otani za Yesu Kristu?

PEMPHERO: Kambilanani za nthawi yanu ya cete. Pemphererani m'busa wa mpingo wanu. Onjezani maina a anthu otaika pa m'ndandanda wa maina azinthu zofunika kupepherera.

KUCITIRA UMBONI: Gwiritsani dzanja kusonyeza momwe tingakhalire mu Mau a Mulungu. Mtsogoleri wanu adzakuthandizani ndi malemba. Kambilanani za mabvuto omwe inu munapeza pamene munali kuphunzitsa nkhani ya **ULALO WOLOZA KUMOYO WOSATHA**. Bweretsani bwenzi wanu yemwe sali mkristu ku Kacisi pa tsiku la Mulungu lirikudza.

PHUNZIRO 7

MAU APAMTIMA: Macitidwe 17:11; Cibvumbulutso 1:3

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: KUSO NKHANA PAMODZI

Ahebri 10:24-25 Ndicizolowezi cabwino ku.


Macitidwe 2:43-47 Okhulupilira anagawirana zinthu zao ndi

Mateyu 18:20 Ngati okhulupilira akhala pamodzi Yesu Kristu ali.

Yohane 13:34-35 Yesu Kristu atilamulira kuti

PEMPHERO: Pemphererani mpingo wanu kuti ukhale naco cizolowezi cakusonkhana pamodzi kawiri kawiri.

MTANDA WAMOYO -- KUPEMBEDZA



KUPHUNZITSA

5. Cala cacisanu, cisonyeza kugwiritsa Buku Lopatulika MAU mdzanja lanu ndipo cisonyeza kugwiritsa nchito MAU mu moyo wathu. Yakobo 1:22 ikuti, “KHALANI AKUCITA MAU, OSATI AKUMVA OKHA, NDIKUDZI-NYENGA NOKHA.”

Kulandira mumitima mwathu MAU nkofunika komabe siti-ngakhale mu MAU molimba kufikira titawagwiritsa nchito mu moyo wathu.

KUCITIRA UMBONI: Gwiritsirani nchito dzanja kusonyeza momwe tingakhali mu mau a Mulungu. Pitani mukacezere Mkristu amene mwa-ona kuti wabwerera kumbuyo mu umoyo wace.

PHUNZIRO 8

MAU APAMTIMA: Masalmo 119:11; Yakobo 1:22

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: UDINDO WA M'KRISTU

Luka 6:38 Patsani anzanu zinthu ndipo Mulungu

.....

2 Akorinto 8:1-5 Mipingo inapereka ngakhale inali

.....

2 Akorinto 9:6-8 Mulungu akonda munthu wopereka

.....

Miyambo 3:9-10 Lemekeza Yehova ndi

PEMPHERO: Pemphererani zopereka za ca khumi canu pamodzi ndi zimene mupereka kwa Mulungu.

KUCITIRA UMBONI: Sabata lino gwiritsirani nchito DZANJA kusonyeza m'mene tingakhali mu Mau a Mulungu.

Lembani nkhani ya umboni wa moyo wanu ndipo mubweretse nkhaniyo ku nyumba komwe mukumaniranako.

Mitu ya nkhani:

1. Moyo wanga ndisanatsatire Yesu.
2. Momwe ndinadziwira kuti Mulungu anali kulankhula ndi ine.

3. Momwe ndinakhalira Mkristu.
4. Tanthauzo la Cikristu kwa ine.

PHUNZIRO 9

MAU APAMTIMA: Luka 14:27; Agalatiya 2:19-20 Bwezirani malemba a DZANJA.

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: MZIMU WOYERA MU MOYO WANU

Yohane 14:25adzakuphunzitsani inu zonse.

Macitidwe 1:8 Mzimu Woyera akupatsani mphamvu yakutumikira kuti?.....

Agalatiya 5:22-26 Kodi zipatso za Mzimu Woyera ndi zotani mu moyo wathu?

PEMPHERO: Pempherani ndi mnzanu sabata liri lonse. Ndi nthawi yanu tsopano kutsogolera gulu lanu kuphunzitsa maphunziro awa. Pemphani Mulungu kuti akutsogolereni posankha anthu asanu ndi m'odzi amene mudzaphunzitsa.

KUCITIRA UMBONI: Fotokozani nkhani ya umboni wa moyo wanu ndi Mulungu ku kalasi lanu. Mtsogoleri alenge MTANDA WA MOYO ndikufotokoza tanthauzo lace. Bweretsani bwenzi amene anataika ku kacisi sabata lamawa.

Pamene ndagwira buku langa Lopatulika ndi cala canga coyamba (1) ndi cala canga ca cikulu (5) nditha kugwira. koma sindidzatha kugwiritsa mwamphamvu. Funsani wina abwere kudzalanda bukulo mutagwira ndi zala zanu ziwiri. cacikulu (5) ndi cacing'ono (1).

2. Cala caciwiri (2) citationetsa njira inanso imene tingasungilemo mau a Mulungu mu mitima yathu - KUWERENGA.

Cibvumbulutso 1:3 ikuti, "WODALA IYE AMENE AWERENGA MAU A CINENEROCO, NASUNGA ZOLEMBEDWA MOMWEMO."

Kufumbata kwanga Buku Lopatulika sikuli kolimba kufikira tsopano. (Yesani kufunsa akulandeni Buku Lopatulika mutagwira ndizala zanu zitatu. (1) (5) ndi (2).

3. Cala cacitatu citationetsa njira yozama yodziwira MAU A MULUNGU. KUSANTHULA.

Macitidwe 17:11 ikuti, "AMENEWA ANALI MFULU KOPOSA A M'TESALONIKA, POPEZA ANALANDIRA MAU NDIKUFUNITSA KWA MTIMA WONSE, NASANTHULA MALEMBO MASIKU ONSE, NGATI ZINTHU ZINALI ZOTERO.


Ngati ndi kumwa, ndi kuganiza, ndi kuwerenga ndiponso ndi kusanthula mau ndi cinthu cobvuta kuti wina acotse kufumbata kwanga. (Talolani munthu wina acotse buku lanu Lopatulika kucoka kudzanja lanu.)

4. Cala cacinai citationetsa njira yabwino kopambana yosungiramo mumitima yathu. Kusungira pantima. Masalmo ikuti, "Ndinabisa mau anu mumtima mwanga kuti ndisalakwire INU. Masalmo 119:11.

Tikasunga Mau apamtima yamakhala mwa ife ndipo ifenso tikhale mu MAUWO. Tsopano tingathe kugwiritsa MAU ndipo palibe angatilande. Tayesani kulola munthu wina ayese kukulandani buku, mudzaona kuti mudzagwiritsa ndipo munthu sadzacipeza cinthu capafupi kukulandani.

PHUNZIRO 10

DZANJA



Tikhale ndi Mulungu pafupi ndi ife mu moyo wathu tiyenera kusunga ndi kukhala ndi MAU ACE mu mitima yathu. Dzanja litipatsa citsanzo ca momwe tingakhalire mu MAU A MULUNGU.

1. Cala coyamba cisonyeza njira yoyamba yomwe tilandilamo mau, KUMVA.

Aroma 10:17 ikuti, COMWECO CIKHULUPILIRO CIDZA NDI MBIRI, NDI MBIRI IDZA MWA MAU AKRISTU.

Cala cacikulu cacisanu (5) cisonyeza momwe tiyenera kuganzira pa MAU.

Masalmo 119:97 ikuti, “Ha! NDIKONDADI CILAMULO CANU, NDILINGILILAPO INE TSIKU LONSE.

MAU APAMTIMA: Yohane 8:31, Yohane 15:7
Bwerezani mau onse ndi malemba a nkhani ya ULALO WOLOZA KUMOYO WOSATHA.

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: MPHATSO YA MZIMU WOYERA

Aefeso 4:7 Kwa ife kwapatsidwa mphatso kucokera kwa.....

Aefeso 4:11-12 Kristu anapatsa mphatso zosiyana kwa ife kuti.....

1 Petro 4:10 Tiyenera kugwiritsa nchito mphatso zathu mokomela.....

Aroma 12:6-8 Lembani mphatso zisanu ndi ziwiri (7) zimene zalembedwa mu ndime izi.
.....
.....

PEMPHERO: Pemphani Mulungu akuthandizeni inu kudziwa mphatso zanu zocokera ku MZIMU WOYERA. Pemphererani citso-gozo ca Mulungu pamene muphunzitsa anthu sabata la mawa. Pemphererani ali-yense mwa amene adzapezeka mu kalasi lanu.

KUCITIRA UMBONI: Lengani ndi kulongosola za mtima, MUTU NDI MIYENDO YA MTANDA WAMOYO ku gulu lanu. Kambani nkhani ya moyo wanu ndi MULUNGU ku munthu wotaika sabata lino.

PHUNZIRO 11

MAU APAMTIMA: Yohane 13:35; Yohane 15:8

MAU A MULUNGU A PHUNZIRO LALERO: KUGONJETA ZOTIYESA ZA SATANA.

Aefeso 6:10-13 Mutha kucilimika kwa satana mutabvala
.....

Aefeso 6:14-18 Tibvala zida za Mulungu mu
..... pakupempha thandizo la Mulungu.

Ahebri 2:18 Yesu angathandize munthu aliyense woyesedwa ndi satana pakuti iye ana
.....

1 Akorinto 10:13 ali wokhulupirika, amene sadzalola inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza.

PEMPHERO: Pempherani kuti Mulungu akupatseni mphamvu yakukana ndi kugonjetsa mayesero a satana. Pempherani Mulungu kuti adalitse kalasi lanu lomwe inu mudzayamba kuphunzitsa sabata lino. Mupemphenso kuti akuthandizeni kukhala wokhulupirika.

KUCITIRA UMBONI: Lengani ndi kulongosola MANJA A MTANDA WAMOYO. Phunzitsani loyamba ku kalasi lanu latsopano.

PHUNZIRO 12

MAU APAMTIMA: Bwerezani malemba onse a MTANDA WAMOYO.

MAU A MULUNGU A PHUNZIRO LALERO: CIFUNIRO CA MULUNGU CA MOYO WANU.

Yeremiya 29:11 Mulungu yekha adziwa
ali nao pa inu.

Aroma 12:1-2 Lolani Mulungu asinthe maganizo anu, mutatero mudzakhala ndi danga lodziwa
.....

1 Atesalonika 5:16-18 Kondwerani.....
Pempherani
Mzonse

PEMPHERO: Pempherani Mulungu kuti akuthandizeni kuzindikira ndikutsata cifuniro cace wa moyo wanu padziko lino la pansu. Pempherani kuti akupatseni danga lakugawirana ndi anzanu nkhanu ya ULALO WOLOZA KUMOYO WOSATHA, CITSANZO CA DZAJA, NDI MTANDA WAMOYO. Pitolizani ndi kalasi lanu latsopano.

KUCITIRA UMBONI: Lengani ndi kulongola MTANDA WAMOYO. PITILIZANI KUPHUNZITSA KALASI LANU LATSOPANO.